NENANI PEMPHERO ILI KWA MULUNGU MWACHIKHULUPIRIRO:

AMBUYE YESU, ZIKOMO KWAMBIRI CHIFUKWA CHA CHIKONDI CHANU CHACHIKULU PA INE. NDIKUVOMEREZA KUTI NDINE WOCHIMWA NDIPO NDIKUPEMPHA CHIKHULULUKIRO. ZIKOMO PONDIFERA PAMTANDA KUTI MULIPIRE CHILANGO CHA MACHIMO ANGA. INE NDIKUKHULUPIRIRA KUUKA KWAKO KWA AKUFA. KUYAMBIRA TSOPANO, INE NDIKUDALIRA INU MONGA AMBUYE NDI MPULUMUTSI WANGA. NDIKULANDIRA MPHATSO YANU YA MOYO WOSATHA NDIPO NDIKUPEREKA MOYO WANGA KWA INU. NDITHANDIZENI KUSUNGA MALAMULO ANU, NDI KUTI NDIKHALE WOKONDWERETSA PAMASO PANU. AMENE.

NGATI MUKHULUPILIRA MWA YESU KHRISTU, MUNAKUMANA NDI IZI:

- MULI NDI MOYO WOSATHA NDI MULUNGU.
Pakuti chifuniro cha Atate wanga ndi ichi, kuti yense wakuyang'ana Mwana, ndi kukhulupirira Iye, akhale nao moyo wosatha; ndipo Ine ndidzamuukitsa iye tsiku lomaliza. YOHANE 6:40
- MACHIMO AKO ONSE AKHULULUKIDWA.
(ZAKALE, ZAMAKONO, ZAMTSOGOLO)
Amene anatilanditsa ife kuulamuliro wa mdima, natisunthitsa kutilowetsa mu ufumu wa Mwana wa chikondi chake; amene tili nao maomboledwe mwa Iye, m'kukhululukidwa kwa zochimwa zathu; AKOLOSE 1:13-14
- NDIWE CHOLENGEDWA CHATSOPANO PAMASO PA MULUNGU.
ICHI NDI CHIYAMBI CHA MOYO WANU WATSOPANO.
Chifukwa chake ngati munthu aliyense ali mwa Khristu ali wolengedwa watsopano; zinthu zakale zapita, taonani, zakhala zatsopano.
2 AKORINTO 5:17
- NDINU TSOPANO MWANA WA MULUNGU.
Koma onse amene anamlandira Iye, kwa iwo anapatsa mphamvu yakukhala ana a Mulungu, kwa iwotu, akukhulupirira dzina lake;
YOHANE 1:12

KUCHITA ZABWINO SI NJIRA YA CHIPULUMUTSO, KOMA UMBONI WA CHIPULUMUTSO CHATHU.

Pakuti muli opulumutsidwa ndi chisomo chakuchita mwa chikhulupiriro, ndipo ichi chosachokera kwa inu: chili mphatso ya Mulungu; chosachokera kuntchito, kuti asadzitamandire munthu aliyense. AEFESO 2:8-9

Ine ndine mbusa Wabwino, ndipo ndidziwa nkhosa zanga, ndipo zanga zindizindikira; Monga Atate andidziwa Ine, chotero Ine ndimdziwa Atate: ndipo Ine nditaya moyo wanga chifukwa cha nkhosa. Ndipo nkhosa zina ndiri nazo, zimene siziri za khola ili: izonso ndiyenera kuzitenga, ndipo zidzamva mawu anga; ndipo padzakhala khola limodzi, ndi mbusa mmodzi. Chifukwa chake Atate andikonda Ine, chifukwa nditaya moyo wanga, kuti ndikawutengenso. Palibe munthu andichotsera uwu, koma ndiutaya Ine ndekha. Ndiri nayo mphamvu yakuutaya, ndipo ndiri nayo mphamvu yakuulandiranso. Lamulo ili ndinalandira kwa Atate wanga. Nkhosa zanga zimva mau anga, ndipo Ine ndizizindikira, ndipo zinditsata Ine: ndipo Ine ndizipatsa moyo wosatha; ndipo sizidzawonongeka ku nthawi zonse, ndipo palibe munthu adzazikwatula m'dzanja langa. YOHANE 10:14-18,27-28

PALI MFUNDO ZINAYI ZOFUNIKA KUZIMVETSETSA BWINO LOMWE:

1 MULUNGU AMAKUKONDA.

MULUNGU AKUFUNA KUTI MUKAKHALE NDI MOYO WOSATHA NDI IYE KUMWAMBA.
Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana wake wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira Iye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha. YOHANE 3:16

MULUNGU AMAFUNA KUTI MUKHALE NDI MOYO WOKHUTIRITSA KOMANSO WATANTHAUZO.
Siikudza mbala, koma kuti ikabe, ndi kupha, ndi kuononga. Ndadza Ine kuti akhale ndi moyo, ndi kukhala nao wochuluka. YOHANE 10:10

KOMABE, ANTHU AMBIRI SAKHALA NDI MOYO WATANTHAUZO NDIPO SADZIWA ZA MOYO WOSATHA CHIFUKWA...

2 MUNTHU NDI WOCHIMWA MWACHIBADWA. IZI ZINAMULEKANITSA NDI MULUNGU.

TONSE NDIFE OCHIMWA.
Pakuti onse anachimwa, naperewera pa ulemerero wa Mulungu; AROMA 3:23

Pakuti mphotho yake ya uchimo ndi imfa... AROMA 6:23

PALI MITUNDU IWIRI YA IMFA YOTCHULIDWA M'BAIBULO:

- IMFA MWAKUTHUPI
Ndipo popeza kwaikikatu kwa anthu kufa kamodzi, ndipo atafa, chiweruziro; AHEBRI 9:27

- IMFA YAUZIMU KAPENA KULEKANIDWA KWAMUYAYA NDI MULUNGU
Koma amantha, ndi osakhulupirira, ndi onyansa, ndi ambanda, ndi achigololo, ndi olambira mafano, ndi onse a mabodza, cholandira chao chidzakhala m'nyanja yotentha ndi moto ndi sulufure; ndiyo imfa yachiwiri. CHIVUMBULUTSO 21:8

NGATI MUNTHU ALEKANITSIDWA NDI MULUNGU CHIFUKWA CHA UCHIMO WAKE, NDIYE NJIRA YOTHETSERA VUTOLI NDI YOTANI?

NTHAWI ZAMBIRI TIMAGANIZIRA IZI NGATI NJIRA ZOTHETSERA:
CHIPEMBEDZO, NTCHITO ZABWINO, MAKHALIDWE ABWINO

KOMABE, PALI YANKHO LIMODZI LOKHA LOPEREKEDWA NDI MULUNGU.

3 YESU KHRISTU NDIYE NJIRA YOKHAYO YOPITIRA KUMWAMBA.

IZI NDI ZIMENE MULUNGU ANANENA.
Yesu ananena naye, Ine ndine njira, ndi choonadi, ndi moyo. Palibe munthu adza kwa Atate, koma mwa Ine. YOHANE 14:6

YESU KHRISTU ANALIPIRA KWATHUNTHU CHILANGO CHA MACHIMO ANU.
Pakuti Khristunso adamva zowawa kamodzi, chifukwa cha machimo, wolungama m'malo mwa osalungama, kuti akatifikitse kwa Mulungu; wophedwatu m'thupi, koma wopatsidwa moyo mumzimu; 1 PETRO 3:18

MULUNGU ALI NDI LONJEZO LA MOYO WOSATHA.
Iye amene akhulupirira Mwanayo ali nao moyo wosatha; koma iye amene sakhulupirira Mwanayo sadzaona moyo, koma mkwiyo wa Mulungu ukhala pa iye. YOHANE 3:36

KOMABE, KUNGODZIWA ZIMENE YESU KRISTU WATICHITIRA SIKOKWANIRA.

4 TIYENERA KUIKA CHIKHULUPIRIRO CHATHU MWA AMBUYE YESU KHRISTU KUTI TIPULUMUTSIDWE.

CHIPULUMUTSO CHATHU CHIMATHEKA NDI CHISOMO CHA MULUNGU KUDZERA MU CHIKHULUPIRIRO MWA YESU KHRISTU.
Pakuti muli opulumutsidwa ndi chisomo chakuchita mwa chikhulupiriro, ndipo ichi chosachokera kwa inu: chili mphatso ya Mulungu; chosachokera kuntchito, kuti asadzitamandire munthu aliyense. AEFESO 2:8-9